


FILE

File



"Proclaiming Christ through the printed word"



BPH
Baptist Publishing House
OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA
P.O. BOX 1995 LUSAKA

Zifaniziro za Yesu

milton cunningham

V-ZM-YT3I

~~B~~ NYA



Zifaniziro za Yesu

Milton Cunningham

- 5) Iri kudza nthawi pamene munthu ali yense adzafunika kupereka umboni wace wa momwe anagwilira nao ncito matalante ace.

-oo0oo-

Kapolo m'modzi yekha yemwe anaganiza kuti mbuye wace anali wouma mtima ndiye yekhayo amene sanagwire ncito. Akapolo omwe anagwira ncito sanaganiza kuti mbuye wao anali "Wouma mtima." Analandira madalitso a mbuye wao, osati cilango cace (cidzudzulo). Kukhulupirika ndi ncito nthawi zambiri zimalandira madalitso.

MAPHUNZIRO:

- 1) Mulungu amapatsa anthu osiyana mphatso zosiyana. Mulungu amapatsa mphatso kwa anthu onse. Sitalante la munthu lomwe liri ndi kanthu. Cofunika ndico cakuti kodi uli kuligwiritsa ncito bwanji talante lomwe Mulungu anakupatsa?
- 2) Mulungutu sapatsa anthu zinthu zazikuru kudzcita mpaka atakhala okhulupirika mu zinthu zazing'ono." Cabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono ndi dzaika iwe pa zinthu zambiri." Mateyu 25:21. Mphatso ya ncito yabwino yomwe yagwiridwa bwino ndiye ncito ina ya iku-ru. Akapolo omwe anagwiritsa ncito matalante ao sanauzidwa kuti kapumuleni ai. Panali cincito cacikuru coti cicitidwe. Muntu ali yense adzigwiritsa ncito talante lace mwa nzeru.
- 3) Ngati simugwiritsa ncito matalante amene Mulungu anakupatsani mudzawataya. Munthu amene alangidwa ndi amene sayesa, "Koma mbuye wace anayankha nati, 'Kapolo iwe woipa ndi waulesi.'" Talante lace linalandidwa kucoka kwa iye nalipatsidwa kwa uja anali nao khumi. Pamene matalante angonyozeredwa amataika.
- 4) Mulungu satifunsa ife ico comwe iye sanatipatsa. Muntu uja wa talante limodzi sanafunsidwa matalante khumi ai. Anafunsidwa comwe anacita nalo talante lace limodzi lija.

ZA M'KATIMU

MUTU	TSAMBA
1 Mafanizo a Yesu.....	1
2 Alendo a M'Kwati.....	7
3 Wofesa ndi Nthaka.....	11
4 Fanizo la Nansongole.....	15
5 Fanizo La Kapolo Wamangawa Wopanda Cifundo	18
6 Fanizo La Mfarisi ndi wa Msonkho....	22
7 Fanizo La Amangawa Awiri.....	26
8 Fanizo La Msamariya Wokoma Mtima....	30
9 Fanizo La Mwana Wolowerera.....	33
10 Fanizo La Ana Amuna Awiri.....	37
11 Fanizo La Phwando Lalikuru.....	40
12 Fanizo La Anamwali Khumi.....	44
13 Fanizo La Matalante.....	48

Pomwepo anadza kapolo yemwe analandira talante limodzi. "Mbuye ndinakudziwani inu kuti ndinu munthu wouma mtima, wakututa kumene simunafesa, ndi wakusonkhanitsa kumene simunawaza; ndinaopa ine, ndinapita, ndinabisa pansi ndarama yanu." Mateyu 25:24-25. Akapolo awiri oyamba aja anatamandidwa ndi mbuye wao. Wacitatu uja sanatamandidwa konse. Mau a mbuye wace anali aukali ndi oza za." Kapolo iwe woipa ndi wa ulesi!" Ndipo mbuye uja anamlanda talante lija.

Nthawi zambiri mumamva anthu akuti anthu onse ali olingana. Mulungu sawerengera anthu amene ali olemera kwambiri kuposa awo amene ali osauka. Mulungutu sawerengera ao amene ali ophunzira kupambana awo amene sanaphunzire. Pamaso pa Mulungu anthu onse ali olingana. Koma anthu onse sali olingana m'mene angagwirire ncito zao. Ena anthu ali okhoza kucita zinthu zina kuposa ena. Anthu ena ali amphamvu kuposa ena. Ena ali alimi abwino kuposa ena. Anthu ena angaimbe myimbo zokongola pamene ena sangathe nkuimba komwe. Ena akonda kugwira ncito mu na ofesi. Ena akonda kugwira ncito kunja. Anthutu ali osiyana. Monga mbuye uja mufanizolo, Mulungu amapatsa anthu mphatso zosiyana. Phunziro lofunika kwa Akristu nali. Kucuruka kwa mphatso zomwe muli nazo sindizo ziri zofunika kwenikweni ai. Comweconso mphatso yomwe muli nayo siri yopambana. Phunziro lofunika ndilakuti kodi uli kucitanji ndi mphatso yomwe Mulungu anakupatsa? Kodi muli kudzigwiritsa ncito kapena muli kudzibisa pansi? Matalante anthu onse ndi mphamvu zathu zonse zidzisiidwa pansi pa ulamuliro wa Mulungu.

Munthu uja amene anapatsidwa talante limodzi sanalionge. Sanali cidakwa. Sanachovere njuga talante lija ai. Cimo lace linali kusaligwiritsa ncito talente lija. Analibe cinyonga cakugwiritsa ncito talante lija. Anali ndi mantha kuti angamwaze limodzi lokha lomwe mbuye wace amapatsa. Sanali wolola kuyesatu kutero. Kuyesatu kunali kofunika. Nthawi zonse kuyesa kumafunika. Kusacita kanthu ndi kulakwa. Kapolo uja sanagwiritse ncito talante lace ndipo analitaya.

FANIZO LA MATALANTEMateyu 25:14 - 30

MAU A PAMTIMA: "Pakuti kwa yense amene ali nazo, ku-zapatsidwa, ndipo iye adzakhala nazo zocuruka: koma kwa iye amene alibe, kudzacotsedwa, cingakhale cimene anali naco." Mateyu 15:29

Munthu wina wa cuma anali kukonzekera za ule-ndo wace. Asananyamuke anaitana akapolo ace. Pamene anafika anawauza za ulendo wace umene anako-aja ndarama. Kwa wina kapolo anampatsa ndarama matalante asanu (ndarama munga ngati mapaundi ci-kwi cimdzi ndi mazana awiri 1,200 kapena kuti a Kwacha 2,400), kwawina anampatsa matalante awiri (mapaundi 480 kapena a Kwacha 960), ndi wacitatu anampatsa talante limodzi (mapaundi 240 kapena a Kwacha 480). Pamene anali kuwapatsa ndarama zija anali kuwauza kuti mudzisamale pamene ine nda-cokapo.

Kapolo uja analandira matalante asanu ana-yamba kugwira ncito ndi kugulitsa. Kapolo ujan-so analandira matalante awiri anayamba kugwira ncito ndi kugulitsa malonda. Kapolo wacitatu anali wo-siyana ndi anzace. M'malo mwakuti agwiritse ncito talante lace limodzi lija iye anapita nakalifocera pansi (kulibisa pansi).

Patapita masiku ambiri mbuye uja anabwera kuulendo wace uja. Pamene anafika anaitana akapolo ace ajanso. Anali kulakalaka kuti aone kuti akapolo aja anacita ciani ndi ndarama zace zija.

Kapolo uja yemwe analandira matalante asanu anakondweretsa mbuye wace pamene anabwera nao matalante khumi. Kapolo ujan-so wa awiri anawirikizapo ace. M'malo mu akubwera nao awiri anadza ndi anai.

MAFANIZO A YESUMateyu 13:10-17; 34, 35

MAU A PAMTIMA: "Cifukwa kwapatsidwa kwa inu ku-dziwa zinsinsi za ufumu wa Ku-mwamba." Mateyu 13:11

Pamene Yesu anali pa dziko lapansi pano ana-gwira ncito kolimba kuthandiza anthu kumvesetsa za njira za Mulungu. Anacita njira zambirim-biri kuyesa kuonetsa anthu onse colinga ndi cikondi ca Mu-lungu. Nthawi zina Yesu anacita zozidzwitsa. Nthawi zina analankhula mau a nzeru. Nthawi zina anali kungofunsa mafunso. Kawiri kawire anacita mafanizo kutsegula mitima ya anthu ku coonadi ca Mulungu.

M'masiku amene Yesu anali pa dziko lino la-pansi aphunzitsi anali kucita zinthu m'mafanizo kwambiri mu ziphunzitsi zao. Ambiri amafanizo ao anali ngati nthanangula (nthano). Yesu sanacita mafanizo munga ngati nthano. Anacita mafanizo kuthandiza kucita coonadi ca Mulungu kuonekera mo-nga ceniceni. Mafanizo a Yesu anali ofewa kuti munthu awamvesetse. Anali kucita ndi zinthu zo-mwe anali kuzimva. Anali apafupi.

Nazi zinthu zina zofunika zoti tidzisunge mumtima pamene tiri kuphunzira zambiri za Mau a Mulungu kupyolera m'mafanizo.

- 1) Mafanizo ndi zithunzi zomwe zithitha-ndiza ife kumvesetsa bwino coonadi ca Mulungu. Tiyeni tiyerekeze Marko 12:33 ndi Mateyu 5:23; M'Marko 12:33 tiwere-nga "Kukonda mnansi wako munga udzi-konda mwini, kuli koposa ao onse amene apereka ndi ku ocera nsembe." M'Mateyu 5:23-24 ganizo limodzimidzi lomweli lafotokozedwa motere. "Ngati uli kupe-reka copereka cako pa guwa, ndipo nthawi yomweyo mukumbukira kuti mbale wako wakukwiira, siya mphatso yako pa guwa pomwepo nupite; coyamba ndikuka gwiri-zana (kukhululukirana) ndi mbale wako, pamenepo nubwerere ndi kupereka mphatso

wako." Vesi ili la mu Mateyu lititha-ndiza ife kuona, bwino kwa mbiri kuposa Marko, za coonadi cimene Yesu ali ku-nena.

- 2) Mafanizo ambiri a Yesu apereka coonadi cimodzi cacikutu coti tiphunzire. Mafanizo angakhale atari pena afupi. Mu maphunziro awa amafanizo tidzafunafuma kupesa coonadi ceniceni. Coonadi ceniceni cingakhale cosiyana mu fanizo lina ndi lina. Zoona zace zina zomwe ziphunzitsidwa mu mafanizo nazi:

- (a) Ena ationetsa njira momwe anthu ena acitira.
- (b) Ena aphunzitsa za ciweruziro.
- (c) Ena za osamalira za zinthu za ena (a Kapita).
- (d) Ena za zinthu zamkangano.
- (e) Ena za Ufumu wa Mulungu.
- (f) Ena za mphatso ndi za kuluza (kumwaza).
- (g) Ena za ucimo.
- (h) Ena za moyo wa Cikristu.

- 3) Mafanizo agwiritsidwa ncito mkhuphunzitsa coonadi mu njira yakuti aliyense adzamva. Atumiki a Mulungu nthawi zambiri amacita zoonetsera kapena nthano kuthandiza anthu ao kumvesetsa bwino Mau a Mulungu. Mafanizo anacititsidwanso mu njira imodzimodzi. Mafanizo onse a Yesu anacitidwa kupanga zithunzi-thunzi zofunika za coonadi ca Cikristu.

- 4) Mafanizo onse a Yesu anali oona ku moyo ndi cilengedwe. Anali zithunzi-thunzi za zinthu zomwe anthu anadziona. Anacokera mu moyo wa tsiku ndi tsiku wa anthu. Yesu kawirikawiri analankhula zinthu zolingana ndi ao amene anali ku mumvetsera.

- 5) Kumasulira kwa mafanizo kuli kofunika kwambiri. Njira yabwino yakumasulira mafanizo ndikulandira nthano yonse monga ngati ndi nthano yoonadi yonena za

- 5) Tidzikhala okonzeka tsiku liri lonse. Tisamataya nthawi yathu kuyang'anira Kristu. Ai. Tidzitaya nthawi yathu kumugwirira ncito kuti pamene adzabwera tidzakhala okonzeka kukomana Naye.

-oo0oo-

Munthu ali yense adzikhala wokonzeka mwa yekha. Simungabwereke ubale ndi Kristu. Anamwali opusa aja sanatha kubwereka mafuta kwa anza ocejera aja. Njira imodzimodzi munthu sangathe kubwereka ubale ndi Kristu. Tsiku liri lonse munthu ali yense adzikonzekera kukomana ndi Kristu. Kukhulupirika ku Mau a Mulungu kumatithandiza mu kukonzekera kwathu.

MAPHUNZIRO:

- 1) Munthu sangacite zomwe amanyozera. Anamwali khumi onse aja anadziwa zomwe zinali kufunika. Asanu a iwo anakonzekera ena asanu sanakonzekera. Kwa awo amene sanakonzekera panalibenso mwai wina waciwiri. Ananyozera zomwe anadziwa kuti zicitike.
- 2) Munthu ali yense adzikhala wokonzeka mwa yekha ngati afuna kudzakhala nao pacikondwerero ca opulumutsidwa pamene Kristu adzabweranso. Kukhala ciwalo ca mpingo sicitanthauza kuti muli okonzeka. Awo okha amene analapa macimo ao nalandira Kristu amene ali okonzeka. Kukhala ciwalo ca mpingo ndi kupulumutsidwa sidziri cinthu cimodzimodzi, (zofanana).
- 3) Yesu Kristu ali kubweranso. Palibe wina ali yense adziwa adzabwera liti! Pamene adzabwera ao onse amene ali okonzeka adzakomana naye. Awo amene ali okonzeka adzapatulidwa kucokako. Anamwali opusa aja akadati-thandiza kuona kufunika kwace kwa kukhala wokonzeka kukomana naye pamene abwera.
- 4) Pamene Kristu adzabweranso anthu onse adzaima pamaso pace. Idzakhala nthawi ya ciweruzo. Anthu opusa adzacotsedwa pamaso pa Mulungu ndi anthu anzeru adzalandiridwa ku phwando la Mulungu.

moyo. Ciweruzo cathu ca pa mafanizo cidzikhazikika pa zimenezi. Mafanizo amaperekedwa mu njira yakuti wakumvetsera uja apange cisankho mu mitima mwace. Atatha kucita cisankho cace acicite m'moyo mwace.

- 6) Zoonadi za mafanizo a Yesu ndi za kwa munthu aliyense ndi mtundu uli wonse wa pa dziko lapansi. Sanalembedwere kwa anthu owerengeka okha ai. Analembedwera kwa ao amene anali kugwili-ra ncito limodzi ndi Yesu. Analembedweranso kwa iwe ndi ine lero. Pamene muli kuwerenga mabuku a Mateyu, Marko, Luka ndi Yohane mungapeze mafanizo amodzimodzi mu mabuku osiyanasiyana. Fanizo limodzimodzi lalembedwa ndi mau osiyana. Musalola kuti ici cikusokonezeni. Sasutsana lina ndi linzace. Athandizana kuonetsa coonadi ca Mulungu.

Mu maphunziro awa a Mafanizo a Yesu tidzafunafuna coonadi ceniceni ca fanizo liri lonse. Tikapeze coonadi cace tidzafuna kucicititsa ncito m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku.

Kukuthandizani inu kumvesetsa bwino Mafanizo a Yesu nau m'ndandanda wa mafanizo omwe anaphunzitsa:

MAFANIZO AUTUMIKI WACE WOYAMBA

"MBIRI YABWINO"

FANIZO:

Anyamata a aukwati	Luka	5:33-35
Zigamba za tsopano pa nsaru za kale	Luka	5:36
Vinyo watsopano mu matumba akale	Luka	5:37-39
Cuma Catsopano ndi Cuma ca Kale	Mateyu	13:51-52
Kukula	Marko	4:26-29
Mbeu Ya Mpiru	Marko	4:30-32
Cotupitsa	Mateyu	13:33
Cuma Cobisika	Mateyu	13:44
Ngale Ya Mtengo Waukuru	Mateyu	13:45-46
Khoka	Mateyu	13:47-50
Wofesa	Mateyu	13: 3-33
Pamasewera a ana	Luka	7:31-35
Womanga Wocenjera ndi Wopusa	Mateyu	7:24-27
Nansongole	Mateyu	13:24-43

Pamene mkwati afika onse amayatsa nyali zao nalowa naye ku phwando laukwati. Okhawo amene anali ndi nyali zoyatsa ndiwo amalowa naye mnyumba. Khomo likatsekedwa palibenso kulola wina ali yense kulowa mnyumbamo, m'mene muli phwando laukwati.

Mufanizo la anamwali khumi asanu anali ocenjera asanu anali opusa. Asanu anali okonzeka asanu anali osakonzekera. Asanu anali ndi mafuta asanu ena analibe mafuta. Pamene mkwati anali kukonzekera kubwera anamwali khumi aja anagona tulo. Pakati pausiku amamva wa mthenga ali kuitana nati mkwati ali kubwera. Mwamsanga anayamba kukonza nyali zao. Anamwali opusa aja anayamba kupempha anzao aja mafuta. Anamwali ocenjera aja nakana pempho lao panena kuti analibe mafuta oti nkuwapatsa anali nao okwanira iwo okha. Cinali cosatheka kwa aja opusa kukagula mafuta. Panali pakati pa usiku ndi awo amene anali ogulitsa malo nda nkuti ali mkati mwa tulo. Anamwali opusa aja anayesayesa kufunafuna mafuta anyali zao. Pamene anali kufuna funa mafuta mkwati anafika. Khomo la nyumba linatsekedwa! Sanakhale nao paukwati!

Mau a Mulungu amatiphunzitsa kuti Ambuye Yesu Kristu adzabweranso kudziko lapansi. Atiphunzitsa ife kuti palibe munthu yemwe adziwa tsiku lace kapena ora lakudza kwace. "Pakuti inu nokha mudziwa bwino kuti tsiku la Ambuye lidzadza monga mbala usiku." 1 Atesalonika 5:2. Ncito yathu ndiyo yakukhala okonzeka. Sitiuzidwa kuti nthawi zonse tidziyang'anira Ambuye. Anamwali amufanizo aja sanalangidwe cifukwa cakuti anagona tulo ai. Anali opusa cifukwa sanali okonzeka. Icit ncofunika kwambiri. Podziwa kuti Ambuye alikubweranso tiyenera kukhala okonzekera kudza kwace. Tifunika kukhala tsiku liri lonse mwa Kristu. Kwa anthu a Mulungu enieni siciri cinthu cobvuta kuti kodi Kristu adzabwera liti. Ali okonzeka kukomana naye.

Ziripo zinthu zina zomwe sitingadzisiye mpaka kumapeto pamene nthawi yatha kale. Zinthu zofunika myoyo yathu zimafunika kuti tidziane TSOPANO! Wa skulu yemwe amalindira mpaka tsiku lotsiriza kuti aphunzire cifukwa ca mayeso amalephera. Munthu yemwe alindira mpaka tsiku lomaliza kukonzekera kudza kwa Kristu adzacedwa.

FANIZO LA ANAMWALI KHUMIMateyu 25:1 - 13

MAU A PAMTIMA: *"Cifukwa cace dikirani, pakuti si-mudziwa tsiku lace, kapena nthawi yace."* Mateyu 25:13

Akuphunzira anali kumuyendetsa Yesu kumuone-tsa kacisi wao wa tsopano. Anali malo okongola kwambiri. Pamene Yesu anayang'ana kacisi wamkuru-yu anauza akuphunzira ace kuti tsiku liri nkudza lo-mwe kacisiyu adzaonongedwa. Iye anati, "Simuona izi zonse kodi? indetu ndinena kwa inu, Sipadzakhala pano mwala umodzi pa unzace, umene sudzagwetsedwa. Mateyu 24:2.

"Mutiuze ife zija zidzaoneka liti? ndipo ci-zindikiro ca kufika kwanu nciani, ndi mathedwe a-nthawi ya pansi pano." Akuphunzira aja anali odera nkha kufuna kudziwa kuyankha kwace. Powaya-nkha funso lao Yesu ananena mafanizo owerengeka. Li-na la mafanizowo ndi fanizo la anamwali khumi. Fa-nizoli linali lakuti lithandize akuphunzira kuona kuti adzikhala okonzeka nthawi iri yonse.

M'masiku pamene Yesu anali pansipano ukwati inali nthawi yodabwitsa kwambiri. Anthu onse am'mudzi amayenda ndi aja okwatirana mpaka kukafika kunyumba yao yatsopano. Anamwali khumi awa amu fanizoli anali akuti adikire ndi mkwatibwi. Pamene anali kulindira mkwati kuti afike anali kubvina ndi kuimba. Panalibe wina ali yense yemwe anadziwa mkwati adzafika nthawi yanji. Pena adzafika mwa-tsopano, pena padzapita masiku owerengeka. Pamene anali kufika munthu anali kuthamanga patsogolo pace nafaula kuuza anthu; "Onani mkwati! Turukani muko-mane naye."

Mwambo wina wa masiku amenewo unali wakuti, ali yense amene ali pa mseu akhale ndi muuni(nyali) yoyatsa. Nyali zao zinali kupangidwa pomabviika nsanza zakale mumafuta ndidzimangirira ku ndondo.

"ANA A UFUMU WA MULUNGU"FANIZO:

Nyumba Yopanda Kanthu	Mateyu 12:43-45
Nsanja Yosatha	Luka 14:25-30
Cilinganizo ca Mfumu ca Nkhondo	Luka 14:31-33
Nzeru Ya Mfumu	Luka 14: 7-11
Mfarisi ndi wa Msonkho	Luka 18: 9-14
Amangawa Awiri	Luka 7:40-49
Kapolo Wopanda Cifundo	Mateyu 18:21-35
Mkuyu Wosabala Cipatso	Luka 13: 1- 9
Kapolo	Luka 17: 7-10
Kapitawo Wonyenga	Luka 16: 1- 9
Wacuma Wopusa	Luka 12:13-21
Wacuma ndi Wopemphapempha	Luka 16:19-31
Msamariya Wokoma Mtima	Luka 10:25-37
Fanizo la Ancito	Mateyu 20: 1-16
Bwenzi pakati pa Usiku	Luka 11: 5-13
Mkazi wa Masiye	Luka 18: 1- 8
Nkhosa Yotaika	Luka 15: 1- 7
Ndarama Yotaika	Luka 15: 8-10
Mwana Wolowerera	Luka 15:11-32

MAFANIZO A YESU A SABATA LACE LOMARIZA

"CIWERUZIRO NDI UFUMU WA MULUNGU"

FANIZO:

Ana Amuna Awiri	Mateyu 21:28-32
Olima munda wa Mpesa Ankhanza:	Mateyu 21:33-41
Phwando Lalikuru	Luka 14:12-24
Cobvala Caukwati	Mateyu 22:11-14
Anamwali Khumi	Mateyu 25: 1-13
Matalante	Mateyu 25:14-30
Ciweruzo Comaliza	Mateyu 25:31-46

-oo0oo-

- 3) Anthu amapanga zowiringura zambiri, koma pali cifukwa cimodzi cokha comwe satsatira Ambuye Yesu. Satsatira cifukwa safunadi kumutsatira.
- 4) Cikondi ca Mulungu ndi ca anthu onse. Palibe wina yemwe akanidwa.

-oo0oo-

Anthu amenewa anali kuika zinthu zao ndi cikondi cao patsogolo pa Mulungu. Anasokonezeka. Anaganizira kuti zinthu zao za dziko lapansizi zinali zofunika kwa mbiri kuposa zinthu za Mulungu.

Anali ngati munthu yemwe agula galimoto la tsopano. Asanagule galimoto la anali wokhulupirika kupita ku calici. Koma pamene anagula galimoto basi osabweranso ku calici. Anati, "Tisanagule galimoto lathu tinali kubwera ku calici pa tsiku la Sunday liri lonse, koma tsopano ai timayendera anansi athu!" Sicimo kukhala ndi galimoto. Koma ngati galimoto litipangitsa kusatsatira njira ya Mulungu - ndi cimo! Pamene anthu afunadi Mulungu, amaiwala zowiringula zao.

Cifukwa cakuti aja onse amene anaitanidwa anakana, ambuye anatuma akapolo ace kukatenga aja onse amene anali osafunika. Ayuda anali kunyonza munthu ali yense yemwe sanali mu Yuda. (Anali kucedwa Akupja). Anakhulupirira kuti mapangano a Mulungu anali a Ayuda okha basi. Iwo anali anthu okondeka ndi Mulungu.

Mufanizo ili Yesu anali kusonyeza Ayuda kuti akunja adzatenga malo ao mu phwando la Mulungu. Ali yense adzaitanidwa kalandira kuitana kwa Mulungu kwakukuru.

Mulungu sakonda Ayuda cabe. Cikondi ca Mulungu ndi ca anthu onse. Onse aitanidwa ku gome lace.

MAPHUNZIRO:

- 1) Tikhale osamala kuika Mulungu kukhala woyamba. Zinthu zabwino zingakhale zithu zoi-pa ngati zidzala m'myoyo yathu kwambiri kuposa Mulungu.
- 2) Madalitso a Mulungu aperekedwa kwa anthu onse, koma okhao amene alandira kuitana kwace amalandira.

MUTU 2

ALENDU A M'KWATI

Luka 5:33-39; Mateyu 9:14-17; Marko 3:18-22

MAU A PAMTIMA: "Ndipo palibe munthu amatsanulira vinyo watsopano m'matu - mba akale: pena vinyo adzaphulitsa matumba, ndipo aonongeka vinyo, ndi matumba omwe: koma vinyo watsopano amatsanulira m'matumba atso-pano." Marko 2:22

Yesu anali ku phwando. Kunali kunyumba ya Mateyu. Inali nthawi yodabwitsa. Nkuti Mateyu atangopereka mtima wace kwa Kristu. Cimwemwe comwe anacipeza mwa Kristu cinali cacikuru kotero kuti anafuna anzace adziwe. Kuwathandiza kudziwa za kuyeretsa ndi kukhululukira komwe anakupeza mwa Kristu anawaitana ku phwando ku nyumba yace. Baibulo limationetsa kuti abwenzi ambiri a Mateyu anali "Amisonkho ndi Ocimwa." Ici sidadamletsa Yesu kupitako. Inali nthawi yomwe anali kuiyang'anira kwa nthawi yaitari. Inali nyengo ina yakugawa zodabwitsa zace za cikondi ca Mulungu.

Pamene alembi ndi Afarisi anamva ici anafunsa mafunso ambirimbi. Sadatha kumvesetsa kuti munthu wacipembezo angakhale limodzi ndi anthu ocimwa.

"Cifukwa ninji muli kudya ndi kumwa ndi anthu ocimwa ndi amisonkho?" Anafunsa. (Luka 5:30).

Iwo anati, "Akuphunzira a Yohane amasala kudya ndi kupephera, comweconso akuphunzira a Afarisi, koma anu akudya ndi kumwa." (Luka 5:33).

Yesu anawayankha iwo pakuwafunsa funso. "Kodi mungaletse alendo a m'kwati kudya pamene m'kwati ali nao limodzi?" Yesu anali kunena kwa alembi ndi Afarisi kuti kwa akuphunzira ace iyi sinali nthawi yakusala kudya - koma nthawi yakudya phwando. Inali nthawi ya cikondwerero!

Alembi ndi Afarisi anali kukhala pansi pa malamulo a Mose. Panali zocitika zazikuru zitatu m'moyo wacipembezo ca Ayuda. Zinali kupereka za cifundo, kupemphera ndi kusala kudya. Kulingana ndi cilamulo ca Mose kusalo kudya pa caka conse linali tsiku lokha Tsiku la Kuteteza. Komabe, Ayuda ena acangu anaonjezerapo masiku ena akusala kudya. Colinga cao conse ca cipembezo cinamangidwa cabe pakusunga malamulo.

Uthenga umene Yesu analalikira sunamvera malamulo ao. Ciyuda cinali cinthu cina. Ukristu sunatsamira pa malamulo koma pa m'mzimu wa munthu. Cipembezo ca alembi ndi Afarisi sicinali kanthu konse koma malamulo okhaokha, Munalibe cikondwerero mu cipembezo cao. Inali ncito. Uthenga umene Yesu analalikira unali wosutsana ndi zime-nezo. Cace cinali cipembezo cacimwemwe. Cina-zadza mtima wa munthu ndi cikondwerero cacikuru. Cinali ngati cikondwerero comwe cimaoneka pa ukwati. Werengani Yohane 3:29.

Alembi ndi Afarisi anasala kudya cifukwa cinali cofunikira ndi malamulo ao. Akuphunzira a Yohane Mbatizi anasalanso kudya. Cifukwa ngakhale kwa iwo cipembezo cinali cenjezo loopsa la cionongeko. Anali ndi nyengo ya "Kuthawa mkwiyo unali kudza." (Mateyu 3:7). Koma kwa akuphunzira a Yesu, ndi m'mkwati, iyi siinalinthawi yakusala kudyakoma kudya ndi kukondwerera.

Funso lenileni lomwe alembi ndi Afarisi anali kumfunsa Yesu linali "Uli ndi m'phamvu yotani yakuswa mwambo?" Iwo sadamvesetse konse za kudza kwace.

Sadabwere kudzaswa malamulo ndi cipembezo cao. Anabwera mu dziko kudzacita zomwe malamulo akale aja sakadacita. Sanabwere "Kudzaononga, koma kudzakhululukira" lamulo. (Mateyu 5:17). Kutengera (kuphatika) Ukristu mu Ciyuda cinali cinthu cosatheka.

"Palibe yemwe amang'amba nsaru yatsopano naika pa nsaru yakale," Anatero Yesu (Luka 5:36). Ngati atero ang'amba nsaru yatsopano ndipo mawanga ace adzakhala osiyana. Simungaonjezere cipembezo catsopano ca Kristu ku cipembezo cakale ca-

munthu ali yense anakana kuitanidwako. Komatu izi ndizo zomwe zinaoneka mu fanizo ili. "Anayamba onse kuwiringula (kupanga zina zozikanira)."

Fanizoli linanenedwa kusonyeza mcitidwe wa Ayuda womwe anali kumcitira Yesu. Linanenedwa kuwasonyeza kupusa kwao pokana kuitana kwa Mulungu. Tiri nao anthu monga awa mpaka lero. Tiona ambiri omwe ali okondweretsedwa ndi zinthu zomwe ali nazo koposa zinthu zosatha. Zinthu zapamwamba za moyo sadzifuna. Ambiri angakhale nazo zinthu zambiri koma zinthu zao sidziwapatsa mtendere. Mtendere ungapezeke cabe polandira kuitana kwa Kristu. Anthu angagwire ncito kupanga ndarama zambiri, koma ndarama sidzidzetsa kukondwa. Kukondwera kumadza kwa awo amene abvomera kuitana kwa Mulungu.

Mulungu anaitana anthu onse kubwera ku phwando lace. Amapereka zinthu zabwino kwambiri kwa awo amene alandira kuitana kwace. Aitana ife kutenga - thandizo lace - citsogolero cace ca myoyo yathu - mtendere wa malingaliro athu - mtima wokondwera - kudzilamulira pa zinthu zomwe tiri nazo - cogonjetso ca paimfa - njira yakupita ku mwamba - moyo wosatha!

Ndi cinthutu coopsa kwa munthu yemwe angofuna zinthu zomwe ali nazo. Anthu ambiri mbiri ali kukana kuitana kwa Mulungu. Alephera kukhala pa phwando la Mulungu cifukwa akana kulandira kuitana kwa Mulungu. Anthuwa alibe zinthu zosatha m'moyo.

Mufanizoli anthu atatu aja anapereka zozikanira zofooka kwambiri. Munthu uja wa munda wace anati anali wokondweretsedwa ndi munda wace. Munthu wa ng'ombe zace zagori analiwokondweretsedwa ndi zomwe anali nazo. Munthu uja wa mkazi wace anali wokondweretsedwa kwambiri ndi cikondi cace ca tsopano. Kuwiringula kwao konse kunali kopusa kwambiri. Anthu amenewa anali ngati anthu akhungu. Anali nao maso akuti aone -koma sadaone.

Tifunika kuonapo kuti palibe mmodzi wa anthu awa amene sanafika kuphwando kuja cifukwa ca zinthu za ucimo. Sicimo muthu kugula munda, kapena ng'ombe za gori. Kapena sikucimwa munthu kukwatira.

FANIZO LA PHWANDO LALIKURULuka 14:15 - 24

MAU A PAMTIMA: "Ndipo mbuye ananena kwa kapoloyo, Turuka, nupite ku miseu ndi njira za kuminda, nuwaumirize anthu alowe, kuti nyumba yanga idzale." Luka 14:23

Munthu wolempera anakonza phwando lalikuru natana abwenzi ace. Monga unaliri mwambo wao, panthawi yacakudya anatuma kapolo wace kukauza aja oitanidwa kuti zonse sakonzeka. Koma comwe cinadabwitsa kapolo uja ndi mwini cuma uja ncakuti onse amene anaitanidwa anayamba kupanga zina zozikanira, (kawiringula).

Woyamba sanatha kubwera cifukwa anali wangogula dziko ndipo anati, "Ndagula munda ndipo ndipita kukaona." Ndi cinthu codabwitsa kuti sanapita kukaona munda uja asanaugule. Analitu munthu wopusa ngati anapereka ndarama zace asanayambe waona munda wace. Ncito yace inali yofunika kwambiri kuposa kuitanidwa kuja.

Wina anagula ng'ombe za magori asanu. Ndi lole kuti ndinke kukadziyesa. Anali wokondweretse-dwa ndi zatsopano zomwe anali nazo kotero kuti analibe nthawi yakupita ku phwando lija.

Wacitatu anati, "Ndakwatira mkazi, ndipo sindikhoza kufika." Sanazindikira kufunika kwace kwa kuitanidwa. Amuna awiri oyamba anayesa kukhala abwino pokana kuitanidwa kuja. Wacitatu yisanayesa konse kunenapo mwa ubwino. Iye anangoti; "Sindikhoza kubwera."

Cioneka cacilendo kuti amuna amenewa anakana kuitanidwa kwao kwa ku phwando. Nthawi zambiri anthu amaitanidwa kukadya cakudya pamodzi ndi anao (abwenzi ao). Nthawi zina sali okhoza kulantira kuitanidwako. Koma ndicobvuta kuona kuti

tsopano ca Kristu ku cipembezo cakale camakolo anu. Moyo watsopano ufuna zoonetzera za tsopano. Mkhali-dwe wakale udzikhala cotitsogolera. Sisamakhala zotibwezera pambuyo.

"Palibe yemwe amaika vinyo watsopano m'matumba akale." (Luka 5:37). Cifukwa ninji kufuna kusunga matumba akale avinyo? Sali amtengo ai. Koma ndi vinyoyo ali wamtengo. Matumba aja akhale cifukwa cabe ca vinyo. M'fanizo lapafupi iri Yesu akuti cinthu cofunika kwambiri ndi coonadi. Coonadi cisamasinthidwa cifukwa ca zolinganiza zina. Cinthu cofunika kwambiri cinali vinyo - coonadi - matumba kapena miyambo sizinali zofunika. Moyo watsopano umene Kristu apereka udzikhala ndi zionetsero za tsopano.

Yesu anadza kudzausa munthu kuti muli zambira mucipembezo koposa kusunga lamulo. Ncito zathu zidzikhala zomvana ndi m'zimu wathu. Kusunga malamulo sikudzampanga munthu kukhala wa Umulungu. Ngati mulibe cikondi m'mitima yathu ca Kristu, simungakhale kupembeza kwenikweni kwa Mulungu. "Mau a m'kamwa mwanga ndi maganizo a m'mtima wanga abvo-merezeke pamaso panu, Yehova, thanthwe langa, ndi mombolo wanga. (Masalimo 19:14).

Cimvano cimeneci cinabwera kupyolera mukulapa kuti macimo, ndi cikhulupiriro ca mwa Kristu. "Cifukwa cace ngati munthu aliyense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala za tsopano. (2 Akorinto 5:17). Kudziwa Kristu ndiko kudziwa kopambana lamulo. Ndiko kudziwa cimwemwe.

Cifukwa cace cakuti munthu alibe cimwemwe ncakuti alibe Kristu - kukhala wopanda m'kwati. Kwa ao amene ali naye m'kwati ayang'ana patsogolo kwa muyaya kodzala ndi maphwando. Moyo womwe Kristu apereka m'dziko lomwe liri nkudza ndiwodzala ndi maphwando cifukwa Mkwati (Kristu) alipo nthawi zonse.

MAPHUNZIRO:

- 1) Kukhala ndi Kristu m'moyo wanu ndiko kukhala ndi cimwemwe ca nthawi zonse.

- 2) Ukristu wosakondwa uli wosatheka pamene tiri pamaso pa Kristu.
- 3) Kupembeza sikuli kupembeza m'maso mwa Mulungu ngati mtima wathu suli mumvano ndi mau athu ndi zocita zathu.
- 4) Ukristu simalamulo oikidwa kuti tidziwasunga ai. Ndi ciyanjano ca m'mzimu wathu ndi Kristu.

-oo0oo-

Amalakalaka kuti adzionedwa ndi anthu. Ndi cobvutatu kuwacita kuti agwire ncito mu munda wa mpesa wa Ambuye. Tiri naonso anthu mu mipingo yathu omwe abwera kudzagwira ncito mmunda wa mpesa wa Ambuye Pamene atha zaka zambiri zopanda phindu. Pamene anamva kuitana koyamba kwa Ambuye anakana. Kumateto kwace anaona kupusa kwace kwa ucimo natembenukira kukagwira ncito mmunda wa mpesa wa Mulungu.

Pali njira yabwino. Ndiyo njira yakubvo-mereza. Ndiyo njira yomwe ikuti, "Inde, Ndidza-pita" - napitadi.

MAPHUNZIRO:

- 1) Malonjezo sadzatenga malo akucita. Mau abwino sadzatenga malo a ncito za bwino. Zomwe ticita zisamakhala zosiyana ndi zomwe tilankhula. Mulungu sali wokondwetsedwa ndi mau. Ali wokondwetsedwa ndi moyo wodzipereka (wobvomeresa).
- 2) Ngakhale cinthu cabwino cingaonongeke ndi njira yomwe munthu acicitira. Ncito za Cikristu zocitika popanda cikondi ca ci Kristu sidzibwetsa cimwemwe.
- 3) Kupembeza komwe sikutikakamiza ife kukhala mwa Kristu tsiku ndi tsiku kopanda pace. Ngati myoyo yathu sinasendezedwe kufupi ndi Kristu kupyolera mu mpingo pali cinthu cina coipa.
- 4) Cikhulupiriro cosaoona mtima cimsogolera ku kusamvera. Kusaoona mtima kumaononga cilakolako cathu cakukhala moyo wa Kristu.
- 5) Lero ndilo tsiku la ali yense wa ife kulowa mu ncito ya Ambuye. Tso-pano ndiyo nthawi - lero ndilo tsiku!

-oo0oo-

Fanizo la Ana Amuna Awiri lomwe Yesu ananena linali la kwa ena a atsogoleri a Afarisi. Yesu nkuti atangolowa mu kacisi ndipo anayamba kumufunsa mafunso. Sadafunsa mafunso cifukwa caku-ti anali okondweretsedwa nazo. Anafunsa mafunso kusokoneza anthu.

Muntu anali ndi ana amuna awiri. Anapita kwa mwana woyamba ndikupempha kuti apite akagwire ncito ku munda wampesa. Mwana uja anauza atate wace kuti sadzapita. Koma patapita kanthawi mwana uja anasintha maganizo ace napita ku munda wa mpesa kuja. Atate anapita kwa mwana waciwire namufunsa kuti apite kukagwira ncito. Mwana waciwiri uja anabvomera kuti adzapita. Koma anasintha maganizo ace nakhala osapita. Funso nali, "Ndani wa awiriwo anacita cifuniro ca atate wace? Mtso-goleri wa a Afarisi anati, Mwana woyambayo ndiye anali mwana womvera." Yesu ananena kwa iwo, "Indetu ndinena kwa inu, kuti amisonkho ndi akazi aciwerewere amatsogolera inu, kulowa mu Ufumu wa Kumwamba." Mateyu 21:31.

Yesu ananena fanizoli kusonyeza njira zosiyana zomwe anthu anali kupita. Mulungu anaitana anthu kupita ndi kukacita ncito yace. (Kukagwira ncito m'munda wace wampesa). Afarisi anabvomera nati adzapita kukagwira ncito koma sadapita. Amisonkho ndi ocimwa anakana kupita koma asasintha maganizo ao napita.

Mufanizo ili palibe gulu liri lonse lomwe latamandidwa. Cifukwa magulu onse analephera kucica comwe Mulungu anafuna iwo kuti acite. Afarisi analephera kukhala omvera cifukwa cacipembezo cao conama. Amisonkho ndi ocimwa analephera cifukwa cakulabadira zokondweretsa za ucimo. Nkuti atatha kuona kuwawa kwace kwa ucimo pamene anabvomera kupita kukacita ncito m'munda wa mpesa.

Fanizoli litithandiza kuona magulu awiri anthu pa dziko lapansi. Gulu lina limalankhula kwambiri koma ncito zao ndi zazing'ono. Gulu lina lilankhula pang'ono koma acita zincito zambiri. Magulu awiriwa tiri nao mpaka lero. Mu mipingo yathu tiri nao anthu omwe ali ngati Afarisi. Amafuna kukhala atsogoleri. Amadera nkhawa kuti akhale nao malo aulemu.

MUTU 3

WOFESA NDI NTHAKA

Mateyu 13:3-23; Marko 4:1-20; Luka 8:5-18

MAU A PAMTIMA: *"Cotero muntu ali yense wa ife adzadziwerengera mlandu wace kwa Mulungu."* Aroma 14:12

Guru lalikuru la anthu linasonkhana kudzamva mau a Yesu. Anali akhala pafupi ndi nyanja. Gurulo linali lalikuru ndithu kotero kuti Yesu anaimea mukangalawa ndikuwaphunzitsa anthu ali ciimire padooko.

"Wofesa anapita kukafesa," anatero Yesu. Mau amenewa anthu anawamvesetsa bwino lomwe. Cioneka kuti pamene, Yesu anali kulankhula iwo anali kuo-nadi munthu ali kufesa mbeu zace m'mbali mwa njira. Wofesa yemwe Yesu anawauza anali ndi nthaka yosiyanasiyana m'munda wace. Anali ndi nthaka yabwino ndiponso yoipa, ya miyala. Pa nthawi yakufesa anafesa pa nthaka yonseyo.

Nthawi yakufesa ndiyosiyana ndi nthawi yakukunkha. Pamene nthawi yakukunkha yafika anthu ambiri amagwira ncito yao pamodzi yam'minda. Pa nthawi yakufesa ndi munthu m'modzi yekha amene amagwira ncito m'munda. Uyu amene anapita kukafesa mbeu anali ndi ncito ya yekhayekha. Siinali nthawi yakukondwera. Inali nthawi yaciyembekezo. Inali nthawi ya cikhulupiriro.

Wofesa amasonkhanitsa mbeu zace nakonzekera kupita kumunda wace. Njira yakupitira ku munda ndiyopita mukanjira. Sikanjira katsopano ai. Ndi kanjira komwe kakhala kali kuyendedwamo kwa zaka zambiri. Nthaka ya m'njira imenei yakhalayouma ngati mwala. Pamene wofesa uyu ali kupita kumunda mbeu zina zinagwa pambali pa njira. Koma mbeu ija sidzakhala pamene paja nthawi yaitari. Mbaleme zina zidzaona mbeu zija ndikudzidya.

Zina mbeu za wofesa uja zinagwa pa nthaka yodzala ndi miyala. Nthaka yapamenepo inali yabwino koma inali yodzala ndi miyala yambiri. Mbeu ikadakula kwa kanthawi, koma nkufa. Panalibe nthaka

yabwino yoti mbeu ija ikulepo. Panali miyala yambirimbiri.

Mbeu zina za wofesa uja zinagwa pa nthaka yabwino koma nthaka ija inali yosasalazidwa bwino. Ndipo pamene mvula inagwa mbeu zija zinamera, komanso udzu ndi minga zinameranso.

Mbeu zina zinagwa pa nthaka yabwino, ndi yosalizidwa bwino. Mbeu zija zinakula. Ndi-kucokera mu mbeu zimenezi panthawi ya ku kunkha, m'mene anthu analandira zakudya zao.

Atatha kuwauza anthu za nthaka ndi mbeu, Yesu anafotokozera fanizoli kwa akuphunzira ace.

"Munthu aliyense wakumva mau a Ufumu, osawadziwitsai, woipayo angodza, nakwatula cofesedwaco mum'tima mwace. Uyo ndiye wofesedwa mbali mwa njira." Mateyu 13:19.

Mbeu ija idagwa panthaka koma sidalowe munthaka. Mbeu imenei Yesu akuti iri ngati anthu ena. Amva Uthenga wacikondi ca Mulungu, koma sadalola mbeu ya Mau a Mulungu, kulowa mumitima yao. Ali nao makutu omvera - koma samva. Aphunzitsidwa kutsutsana ndi Mulungu. Mitima yao ndiyouma ndi malingiliro ao ndi otsekedwa. Werengani Luka 16:31.

"Koma iye amene afesedwa pamiyala, uyu ndiye wakumva mau, ndikuwalandira pomwepo ndikusekera; ndipo alibe mizu mwa iye, koma akhala nthawi ya ing'ono; ndipo pakudza nsautso kapena zunzo cifukwa ca mau; iye akhumudwa pomwepo." Mateyu 13:20-21.

Mbeu imene iri pa nthaka ya miyala inaoneka yabwino kwa kanthawi koma imafa mwamsanga. Mbeu imeni iri ngati anthu amene amanva Mau a Mulungu nakondwera. Sali okondwera cifukwa cakumva Mau a Mulungu, koma cifukwa amva cinthu cina catsopano. Palibe citsimikizo mtima ca kwa Kristu. Palibe kupapa Palibe kubadwanso kwa tsopano. Sali osinthika m'mitima yao. Pamene mabvuto ndi zothetza khama zifika alibe maziko a uzimu. Amangogwa. Naleka.

MUTU 10

FANIZO LA ANA AMUNA AWIRI

Mateyu 21:28 - 32

MAU A PAMTIMA: "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wa kukhukupirira Iye asatayika, koma akhale nao moyo wosatha." Yohane 3:16

Mafanizo ambiri a Yesu anali olunjika kwa Afarisi. Cipembezo cao conama cinacititsa cisokonezo cambiri pakati pa anthu. Anali otanganikwa kucita cipembezo cao kotero kuti anali be nthawi yakukhala a umulungu. Tsiku lina Yesu anena za iwo, "Pakuti iwo amalankhula, koma samacita." (Mateyo 23:3). Zincito zao zonse zinali kucitidwa kuti anthu ena adzione. Nthawi zonse anali kufuna malo aulemu mu macalici (mpingo). Anali kulankhula kwambiri koma zocita pang'ono.

Mkwiyonso wa Yesu unaonetsedwa kutsutsana ndi Afarisi cifukwa ca mcitidwe wao kwa Iye. Anakana kukhulupirira mau ace nagwira ncito zolimba kuletisa ena kuti asakhulupirire. Awatu acipembezo onyengawa anasunga mbali cabe yaing'ono ya lamulo koma sadatha kucita kali konse koonetsa cikondi ndi cilungamo ndi cikhulupiro.

Yesu anati, "Tsoka inu alembi ndi Afarisi, onyenga! cifukwa mutsuka kunja kwace kwa cikho ndi mbale, koma m'katimo iwo adzala ndi kulanda ndi kusadziletsa. Mfarisi iwe wakhungu, yambotsuka mkati mwa cikho ndi mbale, kuti kunja kwace kukhalenso koyera. Tsoka inu alembi ndi Afarisi, onyenga! cifukwa mufanana ndi manda opaka njereza, amene aonekera okoma kunja kwace, koma adzala mkatimo ndi mafupa anthu akufa ndi zonyansa zonse. Comweco inunso muonekera olungama pa maso pa anthu, koma mkati muli odzala ndi cinyengo ndi kusaweruzika." Mateyu 23:25-28.

Ndi cimodzimodzinso Atate wathu wa Kumwamba. Anthu anagasankhe mu nyumba ya atate, koma ici sicinasintha cikondi ca atate. Cikondi ca Mulungu ca pa anthu ciri cimodzimodzi nthawi zonse.

- 3) Cikondwerero comwe cimo libweretsa ndi ca nthawi ya ifupi. Mwana wolowerera anaganiza kuti adzapeza cikondwerero. Ana kondwera mpaka ndarama zace zonse zinatha. Cimwemwe cace conse cinali cacabe. Cimwemwe cokha comwe cimakhala, ndi cimwemwe comwe cipezeka mu cikondi ca Mulungu.
- 4) Mulungu sakana kukhululukira munthu ali yense. Palibe muntu ndi mmodzi yense mu dziko lapansi yemwe Mulungu sadzamukhululukira. Munthu ali yense yemwe atembenuka kucoka ku macimo ace naitana pa Ambuye adzakhululukidwa. "Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire macimo athu, kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse." 1 Yohane 1:9.

-oo0oo-

"Ndipo iye amene afesedwa ku minga, uyu ndiye wakumva mau; ndipo kulabadira kwa dziko lapansi, ndi cinyengo ca cuma citsamwitsa mau, ndipo akhala wopanda cipatso." Mateyu 13:22.

Ici ndico cimaoneka ngati munthu afuna kutumikira Mulungu koma akali cigwirire macino. Munthu sangakule mwa Kristu ndi mtima wosayera. Ndi cithunzi ca munthu amene ali ndi zambiri zomkondweretsa. Zinthu zambiri zima funa nthawi yace, ndipo kawirikawiri zinthu zofunika kwa mbiri zimaunjikana. Njira imodzi yokha yomwe Mau a Mulungu angakulire ndi yakuti mtima uyeretsedwe.

"Ndipo iye amene afesedwa pa nthaka yabwino, uyu ndiye wakumva mau nawadziwitsa' amene abaladi zipatso, nazifitsa, ena za makumi khumi, ena zamakumi asanu ndi limodzi, ena makumi atatu." Mateyu 13:23.

Nthaka yabwino ndiyo nthaka yokulitsa. Ndikucokera mu nthaka yabwino momwe wofesa adzatuta cakudya cace. Mbeu imodzimodziyo idagwa pa nthaka yabwino ndi pa nthaka yoipa. Kusiyana sikuli mu mbeu ai. Kusiyana kuli mu nthaka.

Mbeu sicinthu comwe ciri ca kufa. Iri ndi moyo. Koma moyo uja kuti udzionetsera wokha uyenera kupeza nthaka yabwino ndi yosalala. Mbeu zomwe ziri munkhokwe sidzionetsera moyo. Zifuna nthaka yabwino.

Ndicimodzimodzi ndi mau a Mulungu m'mitima yathu. Mau a Mulungu sali akufa. Ali amoyo. Koma moyo womwe upezeka m'au a Mulungu ungadzionetsera wokha pamene adzalidwa mwa munthu yemwe walapa, ndi kuyere+sedwa.

"Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ocitacita ndi akuthwa koposa lupanga lakuthwa konse konse, napyoza kufikira kugawira moyo ndi mzimu, ndi zimfundo ndi mafuta a m'mafupa, nazindikiritsa zolingirila ndi zitsimikizo za mtima." Ahebri 4:12.

MAPHUNZIRO:

- 1) Zinthu ziwiri sidzingakhale mu mtima wa munthu pa nthawi imodzi. Kukula kwa cimodzi kutanthauza kufa kwa cina. Werengani Marko 12:30.
- 2) Nthawi imaonetsa muntu ali yense ubale wace ndi Kristu. Pamene nthawi yakukunkha yafika okunkha aka adzaona zipatso za nthaka yabwino. Tingapusitse (kunyenga) anthu - koma sitingapusitse (kunyenga) Mulungu. Ama-dziwa zomwe ziri m'mitima yathu.
- 3) Pali mitundu yambirimбири ya nthaka - koma pali mitundu ya anthu iwiri yokha. Kuli ao amene ali kwa Kristu ndi ao amene sali a kwa Kristu.
- 4) Nthawi irinkudza pamene Mulungu adzakolola minda Yace. Mbeu yomwe yakura pa nthaka yabwino idzakunkhida pa nthawi imeneyo.

-oo0oo-

Mtima wace unali wosweka. Cikondi cace ca pa mwana wace sicinasinthe. Anafunitsa mwana wace kubwera kwao.

Ndi cobvuta kwa ife kuyerekeza kukondwera kwace kwa atate uja pamene anaona mwana uja kubwera kwao. Atate uja anathamanga kukakomana naye. Anampyompyona namulandira kwao. Koma atateyo ananena kwa akopolo ace, "Turutsani msanga mwinjiro wokometsetsa, nimumbveke; ndipo mpatseni mphete ku dzanja lace ndi nsapato ku mapazi ace; ndipo idzani naye mwana wa ng'ombe wonenepa mumuphe, ndipo tidye, tisekere; cifukwa mwana wanga uyu anali wakufa, ndipo akhalanso wamoyo; anali wotaika, ndipo wapezedwa." Luka 15:22-24.

Ndicigwirizano cotani comwe anali naco! Mwana anabwerera kwao kwa atate wace. "Ndinena kwa inu, koteru kudzakhala cimwemwe Kumwamba cifukwa ca wocimwa mmodzi wotembenuka mtima, koposa anthu olungama makumi asanu ndi anai mphambu asanu ndi anai, amene alibe kosowa kutembenuka mtima." Luka 15:7.

Ndani ali mwana wolowerera mu fanizo ili? Ndi yemwe amene afuna moyo wa kukhala kutali ndi Mulungu.

Ndani ali atate? Ndi cithunzi ca Mulungu, wokonzeka, wolola, ndi wokhoza kukhululukira.

MAPHUNZIRO:

- 1) Mulungu anapatsa munthu aliyense mphamvu yakusankha. Monga atate mu nthano iyi, Mulungu satikakamiza kucita zomwe afuna. Amatilo la ife kusankha njira yomwe tingayendemo.
- 2) Cikondi ca Mulungu sicisintha. Cikondi ca atate ca pa mwana wace sicidasinthe cifukwa cakuti mwana uja anacoka. Mtima wace unali wacisoni, koma cikondi cace cinali cimodzimodzi. Pamene mwana uja anabwerera kwao sadamdudzule. Analandiridwa mokondwera.

Komatu ndarama zija zidzikadakhala kwa nthawi ya muyaya. Patapita masabata ambiri omwaza ndarama monga adafunira, anazindikira tsiku lina kuti ndarama zace zonse zidatha. Comweconso monga ndarama zija mabwenzi onse anathawa. Sadafuna kukhala naye pomwe analibe ndarama.

Panali cinthu cimodzi cokha cakuti angacite. Mnyamatayu anafunika kupeza ncito. Icituni cinali cobvuta kucita. Munali njala mu dziko lija ndipo cinali cobvuta kupeza ncito pakuti kunalibe ncito zambiri. Patapita masiku ambiri ofunafuna mnyamata uja analowa ncito pa famu. Ncito yace inali yakudyetsa nkumba. Iyitu inali ncito yapansi ndithu yomwe mu Yuda angacite. Anagwera pansipansi ndithu. Kuti adye anali kuyesa kudyako zomwe nkumba zija zinali kudya. Bwanji kusiyana nanga mu khola lankumba ndi mnyumba ya atate wace.

Pamene anali, kugwira ncito mumathope ndi zonyansa mu khola la nkumba anayamba kuganizira za kwao. Anakumbukira bwino momwe anali kukhalira kwa atate wace. Anakumbukira ndi cakudya cabwino bwanji comwe anali naco. Anakumbukira kufunda konse kwa nyumba ya atate wace ndi kukoma mtima kwace. Ndipo "Analingirira mwa yekha."

Icindi cinthu cofunika kwambiri. Anazindikira kuti anali wopusa. Anaona kuti zinthu zomwe anazifuna mu moyo zinali kupezeka kwao. Anacoka kwao kuti akapeze zomwe anali kudzifuna, koma anangopezakuti zomwe anali kufuna zija zinali kwao basi.

"Ndiri kupita kwathu." Walitsiro, wanjara, ndi wa manyazi, anayamba ulendo wace wopita kwao. Pamene anali kupita munjira anaganizira za mau omwe adzalankhula kwa atate wace. "Atate, ndinacimwira Kumwamba ndi pamaso panu; sindiyeneranso konse kuchulidwa mwana wanu; muniyese ine monga m'modzi wa ancito anu. (Luka 15:18-19). Ulamuliro wa atate wace uja sudambvutanso. Anali wolola kucita kali konse malinga ali kwao.

Atate wace anali ndi zolingilira zosiyana. Pamene anangocoka paja atate wace anali kufunisitsa atabwelera kwao. Tsiku liri lonse anali kuyang'ana kunjira kuti aone kapena anali kubwera.

MUTU 4

FANIZO LA NANSONGOLE

Mateyu 13:24 - 30; 36 - 43

MAU A PAMTIMA: "Ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiwo ana a Ufumuwo; ndi nansongole ndiye ana a woipayo." Mateyu 13:38

Fanizo la nansongole ndi fanizo lomwe line-na za zabwino ndi zoipa. Pamene Yesu anali kunena fanizo iri analankhula mau oti munthu ali yense aka damva.

Mlimi anagwira ncito kolimba tsiku lonse. Anafuna kutsiriza kudzala. Pamene anabwerera kunyumba kwace, anali wokondwere cifukwa munda wace wonse unafesedwa. Tsopano, anali kungoyang'anira kudzakunkha zambiri.

Koma pamene anali kugona usiku womwe uja mdani wace anadza nafesa mbeu zoipa. Mbeu zomwe zinafesedwa ndi mdana uja zinali kucedwa: "Tirigu woyerekeza" (wosakhala weniweni). Pamene mbeu izi zinayamba kukula zinaoneka cimodzimidzi monga tirigu wabwino. Ndi anthu owerengeka omwe akadatha kusiyanyitsa pakati pa tirigu wabwino ndi uja woyerekeza pamene anayamba kukula. Koma mbeu zija zitakula kwa kanthawi muntu tsopano amatha kuona "Tirigu woyerekeza."

Anyamata a mlimi uja ndiwo anali oyamba kuona "Tirigu woyerekeza uja m'munda. Atamfotokozera mbuye wao mbiri yoipayi iwo anafuna kupita kukazula nansongoleyo. Mlimi uja anawafotokozera kuti sangatero ai. Ngati adzazula nansongole nayenso tirigu adzazulidwa (adzaonongeka). Anacedwa kuti angadzilekanitse. Mizi yao inakulira limodzi. Ngati angayese kuzula tirigu woipa, akadaononganso wabwino.

Nthawi inali nkudza yomwe adzazilekanitsa. Mbeu za tirigu woyerekeza (woipa) sadzasiidwa ndi tirigu wabwino. Tirigu woipa uja anali wa ululu. Ngati akadadyedwa akadapangitsa anthu cizungulire. Anali wowawa mkamwa.

Ngati tirigu woipa sakadapatulidwa tirigu wabwino akadaonongedwa. Kunkha ndilo linali nthawi ya kupatula (kulekanitsa).

Pamene akuphunzira anamfunsa Yesu kumasulira kwace kwa fanizoli anawafotokozera. Anayankha:

"Wofesa mbeu yabwino ndiye Mwana wa munthu; ndipo munda ndiwo dziko lapansi; ndi mbeu yabwino ndiyo ana a Ufumuwo; ndi nansongole ndiye ana a woipayo; ndipo mdani amene anamfesa uyu, ndiye mdierekezi: ndi kututa ndico cimariziro ca nthawi ya pansi pamo; ndi otutao ndiwo angelo." Mateyu 13:37-39.

Fanizo iri siliri fanizo la malangizo a mpiingo. Ndi fanizo lomwe litiphunzitsa ife za cimo ndi zonyansa ziri m'moyo. Ndi fanizo lonena za moyo. Amagwira ncito kosalekeza. Colinga cace ncakuti aononge. Ncito yace nkupangitsa cionongeko

Udzutu ndi udzu. Sungasinthe. Ziri pankhondo ndi mbeu zabwino. Zimakula m'njira yakuti mlimi sangadziononge osaononganso mbeu za bwino.

Funso lina lomwe anthu amafunsa ndilakuti "Cifukwa ninji Mulungu amalola coipa?" Ngati Mulungu akadakhonjetsa satana ndi coipa dziko likadakhala likondwa. Ngati Mulungu akadafuna kuononga coipa conse cikadaoneka kwa inu nciani? Ngati anthu onse mdziko amene ali osalungama akadaonongeka - kodi mukadapuluma? Yesu anati, nthawi irikudza pamene coipa cidzaonongedwa, koma ino sindiyo nthawiyo!

Cifukwa ninji tiri nao ucimo ndi zoipa mu dziko? Cifukwa ninji dziko liri losiyana ndi mowe Yesu anafunira kuti likhale? Cifukwa ninji nansongole wacizondi ali ndi tirigu wa cikondi? Cifukwa ninji nansongole wacidani ali kupezeka pakati pa a bwenzi? Cifukwa ninji nansongole wakuledzera wacuruka kwambiri? Cifukwa ninji nansongole wakupha (mbanda) apezeka ndi mbeu zabwino za cikondano cacibale? Cifukwa ninji timapeza nansongole m'myoyo yathu yomwe? M'mabanja athu?

MUTU 9

FANIZO LA MWANA WOLOWERERA

Luka 15:11 - 32

MAU A PAMTIMA: "Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, Atate, ndinacimwira kumwamba ndi pamaso panu." Luka 15:18

Fanizo la Mwana Wolowerera lacedwa kuti ndi fanizo lodabwitsa kwambiri m'Baibulo. Ndi cithunzi thunzi cokongola ca cikondi ca Mulungu. Ndi nthano ya munthu yakuukira Mulungu.

Atate anali ndi ana amuna awiri. Tsiku lina mwana wang'ono anaganizira kuti acoke kwao. Anafuna kukhala wa ufulu (womasuka). Anafuna kumacita zodzisankhira iye mwini. Sadafuna atate wace kumamuuza zoti acite. Anauza atate wace kuti ampatse ndarana zomwe zidzakhala colowa cace. Anafuna kupita kwina.

Atate wace wa mwana uja sadayesa kumukhazika ai. Anapatsa mwana wace ndarama zomwe anafuna. Patapita masiku pang'ono mwana uja ananyamuka ule ndo wace. Anali kupita kukakhala moyo wa bwino! Matumba ace anali odzala ndi ndarama. Akadatha kugula kali konse komwe angafune.

Baibulo litiuza kuti "Anapita ku dziko lakutari." Sitiuzidwa ndi kutari kuti komwe anapita. Kunali kwina kwace kutari kucokera kunyumba ya atate wace ndi womasuka kucoka mucifuniro ca atate wace. Tsopano anali womasuka. Akadatha kucita kali konse komwe kadamkomera. Panalibe wina yemwe akadamletsa. Uwu ndiwo moyo umene anali.

Sipanapite nthawi yaitari kuti akhale ndi mabwenzi ambiri acilendo. Poganzira, anaona ngati ndi mabwenzidi. Cifukwa ca Ndarama zace zonse zambiri anthu ambiri anali kufuna kukhala pafupi naye. Anamwaza ndarama zace monga momwe anafunira. Anagula zinthu zonse zomwe zina-kwaniritisa thupi lace.

Funso sindilo lakuti, "Mbale wanga ndani?"
Funso lenileni ndi lakuti, "Kodi ndine mbale wa yani?"

MAPHUNZIRO:

- 1) Wansembe ndi m'Levi uja ationetsa ife kuti tingakhale otanganikwa mumpingo koma nkulephera kuonetsa mzimu woona wa Kristu. Analibe nthawi yakuthandiza.
- 2) Simau amunthu amene aonetsa mzimu weniweni wa Kristu. Munthu amene ali wolola kudzika na yekha kuthandiza ena mu nthawi ya kusowa ndi ye ali Mkristu woona.
- 3) Kukhala wakuphunzira wa Cikristu woona kumadzionetsa kokha kwa anthu onse. Cikondi cabe ca Kristu mu mitima yathu ndico cingatithandize kupambana kudzikonda ndi zopinga. Ngati tikonda awo okha amu mpingo mwathu, mu mtundu wathu, anthu amtundu wathu, tiribe cikondi coona ca ciKristu.
- 4) Wansembe, m'Levi ndi Msamariya onse anali anthu acipembezo. Kusiya nkwakuti Msamariya uja anacititsa cikondi cace ncito.
- 5) Dziko likadakhala labwino koposa Mkristu aliyense akadaya kuthandiza ao amene amzungulira. Tisamasiya cipembezo cathu mu moyo wathu wa tsiku ndi tsiku.
- 6) Kodi ndiwe mbale (Mnansi) wa Yani?

Mu mipingo (calici) yathu? CIFUKWA NINJI? Mbeu yabwino yafesedwa, ndipo satana mwamsanga wadzalitsa munda wonse uja ndi mbeu za mayesero ndi ucimc.

Koma nthawi ya kukunkha irinkudza. Tirigu woipa adzalekanitsidwa ndi tirigu wa bwino pa ciweruziro ca Mulungu. "Pakuti ife tonse tiyenera koonetsedwa ku mpando wakuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika mthupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa." (2 Akorinto 5:10). Mulungu ndiye adzakhala woweruza. Ciweruzo cace cidzakhala coona mtima ndi copanda tsankho. Cidzaulula mtima weniweni wa munthu aliyense. Sitidziwa tsiku la ciweruziro ca Mulungu. Cinthu cofunika kwambiri kwa ife ndico kufunafuna tsiku ndi tsiku, njira ya Ambuye wathu.

MAPHUNZIRO:

- 1) Fanizo ili litiphunzitsa kuti satana ali pancito nthawi yonse mudziko. Palibe munthu angapululumuke ku mayesero ace ndi zoipa zomwe amabweretsa. Amafesa mbeu zace zoipa mumdimba.
- 2) Fanizo ili litiphunzitsa kulimba kwa ce kwakuweruza munthu malinga ndi maonekedwe ace. Ciweruzo comwe cikhazikitsidwa nkulinga kwa maonekedwe akunjira siciri nthawi zonse cabwino.
- 3) Fanizo ili litiphunzitsa kuti tisamakhala acangu mu ziweruzo zathu. Ngati mlimi uja akadafulumura kuweruza nansongole akadaononga tirigu wace.
- 4) Fanizo ili litiphunzitsa za zoonadi za ndithu za ciweruzo. Anthu onse adzaweruzidwa. Werengani Mateyu 13:40.
- 5) Fanizo ili liphunzitsa kuti yemwe angaweruze ndi Mulungu yekha. Werengani Mateyu 13:41-43.

FANIZO LA KAPOLO WAMANGAWA WOPANDA CIFUNDO

Mateyu 18:21 - 35

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa athu." Mateyu 6:12*

"Pakuti ngati mukhululukira anthu zolakwa zao adzakhululukira inunso Atate wanu wa Kumwamba. Koma ngati simukhululukira anthu zolakwa zao, Atate wanunso sadzakhululukira zolakwa zanu. Mateyu 6:14-15.

"Cifukwa cace bvalani, monga osankhika a Mulungu, oyera mtima ndi okondedwa, mtima wacifundo, kukoma mtima, kudzicepetsa, cifatso, kuleza mtima; kulolerana wina ndi mnzace, ndi kukhululukirana eni okha, ngati wina ali naco cifukwa pa mnzace, monganso Ambuye anakhululukira inu, teroni inunso." Akolose 3:12-13.

"Kodzicenjerani nokha; akacimwa mbale wako umdzudzule; akalapa, umkhululukire. Ndipo akakucimwira kasanu ndi kawiri pa tsiku lace, nakakutembenukira kasanu ndi kawiri ndi kunena, Ndalapa ine; uzimkhululukira." Luka 17:3-4.

"Koma mukhalirane okoma mtima wina ndi mnzace, a mtima wacifundo, akukhululukirana nokha, monganso Mulungu mwa Kristu anakhululukira inu." Aefeso 4:32.

Kukhululukira ndiko kuli pakatikati pa Cikiristu. Ambuye anatsimikizitsa za kufunika kwace kwa kukhululukira pamene anali kuyankha funso lomwe linafunsidwa ndi Petro." Ambuye, kodi mbale wanga adzandilakwira nthawi zingati, ndi kumkhululukira? Monga kucuruka ngati kasanu ndi kawiri?" Simon Petro anaganiza kuti nthawi zisanu ndi ziwiri zinali zambiri kuposa momwe zinayembekezedwa. Cifukwa kulingana ndi cilamulo ca Ciyudayenera kukhululukira nthawi zitatu zokha. Cilamulo ca Ciyuda cinati, khululukira nthawi yoyamba - khululukira nthawi ya

Msamariyanso anali kuyenda njira yomwe ija tsiku lomwelo. Pamene anaona munthu wobvulala uja anaimea. Anapita kunali munthu uja nayamba kumuthandiza. Anatsuka mabala ace. Anamanga muja anabvulala, ndipo anamyamulira pa buru wace munthu uja kunka naye ku nyumba ya alendo. Kumene kuja anafunsa wosunga nyumba ya alendo uja kumusalira munthu uja. Anampatsa ndarama munthu wosunga nyumba ya alendo uja namuuzza kuti ngati adzasowa ndarama zina adzabwera nazo.

Msamariya uyutu anali kupita mtunda waciwiri. Asamariya anali ozondedwa ndi Ayuda. Ayuda anali osakomera Asamariya kwambiri. Koma Msamariya wokoma mtima uyu sadaganiza zonzezi. Sadafuna kubwezera coipa ndi coipa. Anabwezera cikondi ku cizondi. Anaona munthu ali kubvutika ndipo anafuna kuthandiza.

"Ndiuti mwa atatuwa, amene uganiza, anali mbale weniwani wa munthu uja anagwa m'manja mwa acifwamba?" Anafunsa Yesu.

Yankho lace linali lapafupi. Msamariya ndiye anali mbale wabwino. "Ici ndico ndifuna kuti ukhale," Anaonjezera Yesu. Ndiyo njira imene Yesu afuna kuti akuphunzira ace onse adzikhalira.

Sitingawanyengeze anthu. Amadziwa ngati tiwakonda moona mtima. Zincito zathu zionetsa ngati tikondadi kapena ai, monga Kristu. Tisangkonda anthu cifukwa tiwadziwa. Tisangkonda anthu cifukwa akhala pafupi nafe. Tisangkonda ena cifukwa ali amtundu wathu. Tidzikonda anthu onse. Awo amene sitiwadziwa, awo amene acokera ku maiko ena, awonso amitundu (makhungu) ina, adani athu.

Cisoni siciri ca mtundu umodzi kapena mtundu wa anthu umodzi. Mabvuto sangobwera kwa oweregeka okha. M'dziko lonse anthu ali ndi mabvuto ndi zothetsa nzeru. Asowa wina kuwathandiza. Ana a Mulungu akadathamanga kukawapatsa thandizo. Ngati tithandiza cabe cifukwa kuti tidziwa ndi ncito yathu, tilephera. Akristu adzithandiza cifukwa ca cikondi mu mtima mwao ca anthu onse. Cikondi ca Cikiristu coona ciri cofewa manja. Ndi cacangu kucita ncito siciri cokhala ndi zinanso zopinga kapena zoletsa.

FANIZO LA MSAMARIYA WOKOMA MTIMALuka 10:25 - 37

MAU A PAMTIMA: *"Mwa ici adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli naco cikondano wina ndi m'zace."* Yohane 13:35

Mzinda wa Yeriko unali mitunda khumi ndi isanu kucokera mu Yerusalemu ndi mtsinje wa Yordano. Mseu wapakati pa mizinda iwiriya unapita kupyola m' mapiri. Unali mseu wosapitapita anthu ambiri. Anthu ambiri anayenda njira imenei ndipo anazolowera tinjira tamiyala. Pamene anali kumvetsera Yesu anamvesetsa zomwe anali kulankhula.

Mnyamata wina wa cilamulo nkuti atangomufunsa funso Yesu. Funso lomwe anafunsa linali lakuti "Mbale (mnansi) wanga ndani?" Yesu ananena fanizo la Msamariya Wokoma mtima poyankha funso lace.

Munthu anali kuyenda kucokera ku Yerusalemu kupita ku Yeriko. Pamene anali kupyola malo ena opanda anthu mu njira muja ambala (acifwamba) anam'menya natenga ndarama zace. Anamsiya pambali pa mseu ali ngati wakufa. Sipanapite nthawi yaitari pamene wa nsembe anapita njira ija. Anaona munthu uja ali kukha mwazi koma iye sadaime. Baibulo likuti, "Analambalala mbali ina." Kapena anali watanganikwa. Kapena anali paulendo wace wopita ku calici. Kapena anali wacedwa. Kaya cifukwa cina ciri conse sadaime kumuthandiza munthu wome nyedwa uja. Anapitirira kukacita zincito zace.

Patapita ka nthawi munthu wina anabweranso njira yomwe ija. Anali mu Levi. Alevi anali anthu odzipereka mu mpingo. Anasankhidwa kukhala apadera kuthandiza a nsembe. Anapereka myoyo yao ku zincito za cipembezo. Pamene anali kufika pafupi ndi paja pamene panagona munthu uja womenyedwa, anapitirira. Ngatinso wansembe uja sadayesa kuthandiza.

ciwiri - khululukira nthawi ya citatu - koma - mlangwe uyo akucimwira nthawi ya cinai. Pakukhulukira nthawi zisanu ndi ziwiri munthu nkuti ali kucita kuposa momwe lamulo linalamulira.

Yesu adamvesera Simon Petro ndipo pomwepo anati, nthawi zisanu ndi ziwiri siziri zokwanira ai, "Sindikuti kwa iwe nthawi zisanu ndi ziwiri, koma makumi asanu ndi awiri kudza kasanu ndi kawiri." Yesu anali kunena kwa Petro kuti panalibe malekezero mu kukhulukira kwa Cikristu.

Tsiku lina mfumu anaitana akapolo ace onse. Anafuna kulankhula nao za mangawa (ngongole) omwe anali nao. Pamene mfumu uja anayamba kusandula anapeza kuti kapolo wina anali ndi mangawa akuru. Mangawa ace anali oposa matalante zikwi khumi (ngati mapaundi mamillion - awiri kapena theka kapena kuti a Kwacha mamillion asanu). Kapolo uja sakadatha kulipira mangawa ace akuru oterewa. Coterofumfu uja anaganiza zakumgulitsa kapolo uja, banja lace ndi zinthu zace zonse zomwe anali nazo. Potero mfumu ija ikadapezapo tindarama pang'ono pokha.

Pamene kapolo uja amamva colinga ca mfumu anagwa pansi napempha mfumu kuti asamgulitse." Ambuye, ndikomereni mtima, ndidzakulipirani ciri conse comwe ndakongola." Mfumu ija inamva cifundo mu mtima mwace nibvomereza pa pempho la kapolo uja. Anamlola iye kupita.

Atangocoka kwa mfumu kapolo uja, anaona munthu yemwe anamkongola ndarama zace. Munthuyu anakongola kwa kapolo uja ndarama zokwana ngati mapaundi asanu (a Kwacha khumi). Pamene kapolo uja anamuona anamgwira pakhosi. "Lipira mangawa ako," anatero. Munthu uja anapempha kapolo uja kuti ampatse nthawi. Koma kapolo uja sadamvera konse. Anamtumiza munthu uja kunyumba ya ndende.

Pamene akapolo ena anaona cidacitikaco anafulumira kukauza mfumu. Mwa nthawi yocopa cabe kapolo wosakhulukira uyu anali ciriri pamaso pa mfumu. "Kapolo woipa iwe! ndinakukhulukira mangawa ako onse aja cifukwa unandililira (kudandaulira); koma iwe sukadacitira cifundo kodi kapolo mnzako, monga ndinakucitira cifundo iwe? Mfumu inaganiza kumcitira kapolo uja monga iye anacitira ena.

Mulungu alitu monga mfumu, Yesu ananena. Ngati anthu saliolola kuwakhululukira awo amene awacimwira sadzadziwa cikhululukiro ca Mulungu.

Cikhululukiro ca Mulungu ndicacikuru kuposa cikhululukiro ca muntu. Mulungu amkhulukira macimo athu onse. Amatipatsa mwai wina watsopano. Mulungu amakhukulukira ngakhale ace omwe pamene atembenukira kwa iye mkulapa ndi cikhulupiriro. Palibe malekezero a cikhululukiro comwe Mulungu apereka. Kukhulukira kwathu konse nkwakung'ono kuyerekeza ndi cikhululukiro ca Mulungu. Ngati sitiri ola kukhulukira ena zolakwa zao zomwe atilakwira, tingayembekeze bwanji Mulungu kutikhulukira zomwe timlakwira iye?

MAPHUNZIRO:

- 1) Munthu adzikhulukira kuti iyenso akhulukidwe. Tidzikhulukira ena mu mzimu wa Kristu. Ngati tilephera kukhulukira ena tisyembekeze cifundo kucoka kwa Mulungu. Ngati tidziwa cikhulukiro ca Mulungu mu mitima yathu tidzakhala olola kukhulukira anzathu.
- 2) Muntu amene sali wolola kukhulukira adziononga yekha. Cizondi cimakhala mu mtima wace ndipo cikondi cimacokamo. Mzimu wosakhulukira uma panga moyo wosakondwa. Ngati cikondi codabwitsa ca Mulungu sicitipatsa kudzicepetse, cimaumitsa mitima yathu.
- 3) Palibe comwe munthu angaticitire comwe tingayerekeze naco zomwe tacitira Mulungu. Zomwe atilakwira ena ziri zocepa kwambiri kuyerekeza ndi macimo athu kwa Mulungu.

- 4) Mkristu ali yense adzitsimikiza kuti zifuniro zace za kutumikira Kristu ziri zabwino. Dama (kudzikuza) kulibe malo mu utumiki wa Cikristu.

-oo0oo-

onse cikondi codabwitsa ca Mulungu. Ambuye Yesu sayang'ana anthu monga momwe ena ayang'anira. Munthu angakhale wosakondedwa ndi anansi ace - koma zija ziribe kanthu ndi cikondi ca Kristu. Mulibe cinyengo mwa iye. Cikondi cace ndi ca onse. Mkazi uja anatembenuka kucoka ku ucimo napeza moyo mu cikondi ndi cikhululukiro ca Yesu. Simoni sanapenye kwa Yesu kuti akhululukidwe. Analephera kuona kusintha mwa mkazi uja. Anamdziwa iye monga mkhazi wocimwa ndipo maganizo ace sanasithe. Bwanji kusiyana ndi Kristu. Palibe cimo lomwe sangalikhulukire. Palibe munthu yemwe ali wosafika cikondi cace. "Idzani kwa Ine," ndiko kuitana kwace kwa ali yense.

Mu fanizo ili Yesu anali kuyesa kumusonyeza Simoni m'mene cikhululukiro ca Mulungu cikhaliira ca thunthu. Cikondi cace ca pa Yesu cinali cacikuru cifukwa macimo ace anali akuru. Anakumbukira kuyereetsedwa komwe anakupeza mu cikondi ca Kristu. Koma, Yesu anati, awo amene sakhulupirira kuti ali ocimwa kwakukuru saonetsa cikondi cacikuru. Munthu amaona kuda kwace kwa ucimo pamene azindikira kuyera kwa Mulungu.

MAPHUNZIRO:

- 1) Fanizo ili litiphunzitsa kuti mulibe kusiyana mu cikondi ca Kristu. Sako-nda owerengeka okha. Cikondi cace ndi cimodzimodzi kwa onse. Mkazi wa mbiri yoipa uja sanali wosiyana, m'maso a Kristu, ndi munthu wa ulemu wa ukuru.
- 2) Kukhululukidwa kwathu kwa thunthu kwa macimo kutsamira nakuzindikira kwathu ucimo ndi kusowa cikhululukiro. Ngati munthu alibe maganizo enieni ozindikira ucimo wace, sadzamva kusowa kwa cikhululukiro.
- 3) Ciyambi ca kumvera ndi cikondi. Ngati munthu sakonda Kristu sadzakhala ndi cilakolako cakumumvera iye. Ngati munthu amkonda Kristu adzafunafuna kumumvera iye.

- 4) Ndi Kristu, palibe malekezere aku khululukira. Zofunikira za cikhululukiro ca Kristu ndi kupapa ndi cikhulupiriro. Cikhululukiro cace ciri kwa anthu onse amene akhulupirira.
- 5) Muntu amene sali wolola kukhululukira ena adziononga iye mwini.

-oo0oo-

FANIZO LA MAFARISI NDI WA MSONKHOLuka 18:9 - 14

MAU A PAMTIMA: "... Pakuti yense wakudzikuza yekha adzacepetsedwa; koma wodzicepetsa yekha adzakulitsidwa." Luka 18:14

Pamene Yesu anali kuyamba utumiki wace wa dziko lapansi Afarisi ndiwo anali anthu padziko lonse lapansi omwe anali acipembezo kwenikweni. Cipembezo, cao cinali cipembezo ca malamulo. Ngati munthu anasunga malamulo anali munthu wabwino. Anayesetsa kutsatira malamulo onse a Mose. Munalibe cimwemwe mu cipembezo cao. Cikhulupiriro cao cinakhazikitsidwa pa malamulo. Afarisi anali ziwalo zolimba kwenikweni mu macalici (mipingo) yao. Anali kupatsidwa ulemu ndi anthu monga ngati atsogoleri acipembezo. Nthawi zambiri anali kukhala pa malo aulemu pamagulu a anza. Cipembezo cao cinali ndi nsonga zazikuru ziwiri:

- 1) Asapweteke munthu wina aliyense.
- 2) Adzikhala okhulupirika mu zincto zao zonse posunga malamulo onse.

Munthu wina yemwe Yesu ananena za iye mu fanizo iri anali wa msonkho. Anali yemwe Zocita zace zinali zosanga za M'farisi. Sanali mtsogoleri mgulu lace. Anali munthu wamba. Sanali kupatsidwa ulemu. Anali kuyang'anidwa ndi Afarisi aja monga ngati wosakhudzidwa (munthu wonyansa). Wa msonkho anali munthu wopanda lamulo wa ntundu wa iye mwini. Anali mu Yuda, koma Ayuda acipembezo aja sanamkonde.

Yesu anauza akuphunzira ace fanizo iri kuwasonyeza mcitidwe weniweni woona wa cikhulupiriro mwa iye. Anali kuyesa kuwaphunzitsa akuphunsira kusiyana pakati pa kusunga lamulo ndi kukhala naco cikhulupiriro.

Mulibe kena kali konse mu fanizo iri komwe kasonyeza kusaona mtima. Onse awiri Mfarisi ndi Wa-

Munthu uja amene anawakongola ndarama sanadera nkha-wa. Anawauza kuti iwalani ngongoleyi. Sanafunenso kuti amulipire konse ai. "Isopano," anatero Yesu, "Ndiuti wa awiriwa yemwe adzamkonda kwambiri?" Ndiganza uja amene anamkongola zambiri," Anayankha Simoni.

Ndi cimodzimodzi ndi mkazi uyu anatero Yesu. "Kodi umuona mkaziyu? Ndinalowa mnyumba yako, sunandipatsa madzi osamba mapazi anga, koma wanyowetsa mapazi anga ndi misozi yace nawapukuta ndi tsitsi lace. Sunandimpyompyona, koma kuyambira paja ndinalowa muno sadaleka kumpyompyona mapazi anga. Sunazodza mutu wanga ndi mafuta, koma wazodza mapazi anga ndi mafuta. Coteri ndikuuza iwe, macimo ace, amene ali ambiri, akhululukidwa, cifukwa anakonda kwambiri; koma iye amene wakhululukidwa pang'ono, amakonda pang'ono." Luka 7:44-47.

Fanizoli litithandiza kuona mcitidwe wa anthu atatu osiyana. Litithandiza kuona khungu (kusaona) la mzimu lomwe linali ndi Simoni. Monga Mfarisi anali wodzilungamitsa yekha. Anali wonyada. Ngakhale anaitana Yesu m'nyumba mwace analephera kuona cikondi ca Kristu ca kwa anthu onse. Anali wokwanitsidwa ndi iye yekha. Analibe malingaliro a ucimo. Anali nao maso kuti aone - koma sadaone.

Mkazi uja ali wosakhala monga Simoni. Angakhale kuti anali kuzondedwa ndi anthu, koma Yesu anamkonda iye. Cifukwa anadziwa kuti Kristu sadzambweza, anadza kudzaonetsa cikondi cace. Cikondi conse coona ca kwa Mulungu ndi mapeto a zinthu ziwiri:

- 1) Kuzindikira ucimo mu mtima mwa munthu.
- 2) Ndi lonjezano la kukhululuka ndi kukhululukidwa.

Mkazi uja anali nazo zonse ziwirizi. Kuonetsera kwace kwa cikondiku sicinali cifukwa cace cakuti akhululukidwe - cinali cionetsero cakukhululukidwa kwace. Cikondi coonadi ca pa Kristu cidzizonetsera cokha. Sicingabisidwe.

Munthu wacitatu yemwe timuona mu fanizo ili ndi Kristu. Kristu anadza mu dziko kudzaonetsa anthu

FANIZO LA AMANGAWA AWIRILuka 7:36 - 50

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo Iye anatikwa mkaziyo, Cikhulupiriro cako cakupulumutsa iwe;muka ndi mtendere."* Luka 7:50

Simoni anali Mfarisi. Anaona Yesu pamene anali kuphunzitsa ndi kuyenda ndi anthu. Ngakhale Afarisi sadamkonda Yesu, Simoni adamfunsa Yesu kupita ku nyumba yace. Yesu analandira kuitanidwako. Ndi nthawi imene anali kudya ndi Simoni pamene ananena fanizoli.

Pamene Yesu analowa mnyumba ya Simoni, anakhala pa gome kudya. Pamene anali kudya mkazi analowa mcipindamo. Cinaoneka kuti anthu ambiri anamdziwa mkaziyu. Ngati sadamdziwa, anadziwa mbiri yace. Cifukwa anadziwika kuti anali mkazi waciwerewere. Anabwera ku nyumba ya Simoni cifukwa anafuna kuona Yesu. Pamene anali kulowa ananyamula kabokosi kakang'ono kopangidwa ndi mwala. Kanali kadzala ndi mafuta onunkhira kwambiri.

Pamene anaimea pafupi ndi Ambuye anayamba kulira. Misozi yace inagwa pa mapazi a Yesu. Cinali cinthu cokomadi kuona pamene anawerama napukuta mapazi ace ndi tsitsi lace lalitari. Anawampyompyona natira mafuta onunkhira aja.

Onse amene anali mucipinda muja anaona mkazi uja pamene anali kudzoza Yesu. Simoni anati "Ngati munthu uyu anali mneneri, akadadziwa kuti ndi makazi wotani amene anali kumugwira lye, cifukwa ndi wocimwa." Luka 7:39.

Pomuyankha Simoni Yesu ananena fanizo la amangawa awiri. Kunali anthu awiri. Anthu onse awiriwa anakongola ndarama kwa munthu m'modzi. Wina anakongola mapaundi makumi asanu (100 K) ndi wina maupaundi asanu (10 K). Pamene nthawi inafika yoti amuna aja alipire ndarama zija anakongola, amuna aja analibe ndarama.

msokha anali oona mtima. Koma kuona mtima sikuli kokwanira! Munthu angakhale woona mtima koma nku-sowa Ufumu wa Mulungu. Angakhale woona mwacabe.

"Mfarisiyo anaimirira napemphera izi mwa yekha, Mulungu, ndikuyamikani kuti si-ndiri monga anthu onse ena, opambapamba, osalungama, acigololo, kapenaso monga wamsonkho uyu; ndisala kudya kawiri sabata limodzi; ndipereka limodzi la magawo khumi la zonse ndiri nazo." Luka 18:11-12.

Mfarisi anapemphera "Ndikuyamikani," Koma munalibe mzimu weniweni wa kuyamika. Mtima wace unali wodzala ndi kunyada kuti angakhale wotha kuyamika. Sanali kuyamika cifukwa ca madalitso a Mulungu. Anali kuyamika cifukwa "Sanali monga onse ena anthu." Anali wokondwera yekha ndi zinthu zomwe anazicita. Anakana kudziyesa yekha ndi miyeso wa Mulungu. Anadziyesa yekha kulinganiza ndi miyeso ya anthu ena."Mtima wace unadzala ndi cikondi ca iye mwini kotero kuti munalibe malo oti cikondi ca Mulungu cingakalemo. Dyera lace la iye mwini la kunyada linambera cikondi ca Mulungu ndi moyo.

Wamsonkho uja anali munthu wosonkhetsa msonkho. Anali Muyuda. Sanali kukondedwa ndi Ayuda ena cifukwa ca ncito yace. Anaganiza kuti sicinali cinthu cabwino kuti Muyuda adzisonkhetsa msonkho kupereka ku boma lina. Anali pansi pa ulamuliro wa Boma la Aroma. Wa msonkho uja anali kugwirira Aroma ncito yosonkhetsa msonkho. Cifukwa ca ici sanalikukondedwa ndi anthu am'dziko lace.

Pamene Mfarisi anapemphera munseu anafuna kuti anthu onse amuone. Anali kufuna kuti onse aone kuti anali wokhulupirika pakusunga malamulo acipembezo. Anapemphera mofuula kuti onse amumve.

Wamsonkho uja anafuna Mulungu cabe kuti amve pemphero lace. Pamene anapemphera anacoka pagulu la anthu. Sanafuna kuti ena amuone. Sanayesa kuti anthu ena aceuke. Si Sanapemphere cifukwa ca lamulo. Anapemphera cifukwa anafuna kutsikidwa ndi cikhululukiro ca Mulungu.

Pamene anaitanira kwa Mulungu anawerama mutu wace pansi napemphera pemphero lapafupi. "Mulungu, mundicitire cifundo ine wocimwa!" (Luka 18:13). Ndi mtima wodzicepetsa anayang'ana kwa Mulungu kuti ampulumutse kucokera ku ucimo.

Mfarisi uja anali kucoka pa ena cifukwa ca cilungamo ca iye mwini. Wamsonkho uja anapatuka pa ena cifukwaca ucimo wace mwini.

Mfarisi uja anali wonyada osati kwa zinthu zokha zimene sanazicite. Analinso wonyada cifukwa ca zinthu zomwe anazicita. Anasala kudya kawiri sabata limodzi. Anapereka ca khumi ca zinthu zonse anali nazo.

Mtima wa wamsonkho sunali wodzala ndi kunyada. Mtima wace unadzala ndi cizindikiritso capansi ca kucimwa. Anali kuzindikira za kucimwira Mulungu kumene anacita. Mtima wace unali wodzala ndi cisoni ndi kuwawidwa cifukwa ca macimo ace. Pamene anapemphera sanaculapo zinthu zimene anacita. Anali ndi mtima wakulapa.

Kunyada kunamsiyanitsa Mfarisi uja ndi Mulungu. Kudzicepetsa kunasendeza Wamsonkho uja pafupi ndi Mulungu. Palibe ciyembekezo kwa anthu amene akhala ngati Mfarisi uja. Cilungamo ca iwo eni cimaononga ciyembekezo conse. Mzimu wace mwini yekha wakunyada sunampatsa kanthu koma ubwino wonyanga. Koma ngati Mfarisi uja akadangotsegula maso ace naona mzimu wa kudzicepetsa kwa Wamsonkho uja. Comwe Mfarisi uja anasowa Wamsonkho uja anali naco, anali ndi Mtima wosweka ndi wakulapa modzicepetsa.

MAPHUNZIRO:

- 1) Fanizo ili litiphunzitsa kuti kuli zambiri ku Umulungu koposa kungosungana malamulo. Alipo ambiri omwe akhulupirira kuti Mulungu awakonda, cifukwa sapha anthu, sacita cigololo, samwa mowa. Mulungu satikonda cifukwa ca zinthu zomwe siticita. Timazindikira cikondi cace pamene TICITA zimene Anatilamulira ife ife kuti ticite.

- 2) Fanizo ili litiphunzitsa kuti kuli zambiri ku Umulungu kuposa kungodziwa ciphunzitso ca mpingo. Munthu angadziwe ziphunzitso zonse za mpingo wao koma osakhalabe ngati wofanana ndi Kristu. Nthawi zambiri onyenga amacita ncito za cangu m'mpingo. Ciyanjano ndi Kristu siciri muciphunzitso ca mpingo. Ndi mapeto akulapa kwathu macimo ndi cikhulupiriro mwa Kristu.
- 3) Fanizo ili litiphunzitsa kuti zincito sidzionetsa nthawi zonse zomwe siri mu mtima mwathu. Zincito zinapanga Mfarisi uja monga ngati munthudi wa Mulungu, koma mtima wace unali kutari ndi Mulungu. Kupita ku calici, kupe-reka ca khumi ku mpingo, kubatizidwa, zinthu izi sidzipanga munthu kukhala wabwino. Kristu yekha yemwe akhala mwa ife ndiye atipanga a Umulungu. Kodi ndi ciani comwe timacikonda kwambiri? Mumakonda Kristu koposa kanthu kena kali konse?
- 4) Fanizo ili litiphunzitsa za mphamvu ya kunyada. Kunyada kumawasiya anthu ambiri kutari kucoka kwa Mulungu koposa cimo lina liri lonse. Litiphunzitsa za madalitso omwe Mulungu amape-reka kumtima wodzicepetsa.
- 5) Fanizo ili litiphunzitsa kuti pemphero lomwe limakhala ndi ncito liri kutsamira kwa moyo wa uyo amene ali kupe-mphera. Werengani Yakobo 5:16.

-oo0oo-